

**Nkhani za M'makalata za  
Dziko Lonse Lapansi**

**Yerusalem Watsopano**

**Matchalitchi Dziko Lonse**

**Mbusa Tony Alamo**

**Fuko La Chikhristu La Alamo**

**Volume 18800**

# KHRISIMASI NDI CHIPULUMUTSO

**Yolembedwa ndi Tony Alamo**

Kunali kutatsala miyezi isanu ndi inayi kuti lifike tsiku la Khrisimasi yoyamba, kubadwa kwa KHRISTU. MULUNGU anali, mwanthawi zonse, atakhala pa mpando WAKE wachifumu KUMWAMBA.<sup>1</sup> “Ndipo IYE [mngelo wa MULUNGU] anandiwonetsa [Yohane, Mtumiki] mtsinje woyerwa bwino wa madzi a MOYO, woyerwa ngati galasi lonyezimira.” Genesesi 1:7 akuti, “Ndipo MULUNGU analenga mlengalenga [immene mumagawa pakati pa madzi akumwamba ndi madzi apanthaka], ndikugawa madzi amene anali pansi pa mulengalenga kuchokera kwa madzi amene anali pamwamba pa mulengalenga [madzi amenewa pamwamba pa mlengalenga ndi MZIMU WOYERA, madzi a MOYO, amene MULUNGU amatumiza kwa wokhulupilira mwa KHRISTU aliyense<sup>2</sup>]: ndipo kunali [ndipo kudakali] chomwecho.”

Komanso, madzi amenewa siodetsedwa, koma aukhondo kwambiri

ndi “woyera ngati galasi lonyezimira, akudutsa kuchokera ku mpando wachifumu wa MULUNGU ndi wa NKHOSA. M'katikati mwa njira ya madzi amenewa, ndipo kumbali zonse za mtsinje, kunali iko mtengo wa MOYO, umene unabekela mama-na a zipatso khumi ndi ziwiri, ndiku-kolora zipatso zake mwezi uliwonse: ndipo masamba a mtengo anali ochilitsira maiko” (Chivumbulutso 22:1-2).

Mtsinje umenewu, umene unabekela YESU m'mimba mwa Mariya, ndi mtsinje womwewo umene kumapeto udzabeleke KHRISTU pamodzi ndi ATATE mwa MZIMU kunka mwa wokhulupilira aliyense wam'tsogolo mwa KHRISTU.<sup>3</sup> MZIMU ameneyu ndi mtsinje umene udzauktse aliyense kwa akufa patsiku lomaliza,<sup>4</sup> ena ku MOYO wosatha, ndipo ena ku chiwonongeko ndi chilango cha muyaya (Danieli 12:2, Chivumbulutso 20:6).

Chivumbulutso 14:10-11 akunena za iwo amene adzazunzike ndi chilan-



*M'busa Alamo ndi malemu mkazi wake Susan pa porogaramu yayo yachiKhristu yapakanema yadziko lonse Chithunzi—1974*

go chamuyaya: “Omwewo adzamwa vinyo wa mkwiyo wa MULUNGU, umene umathiridwa wosasakaniza mu chikho cha mkwiyo WAKE wobwera chifukwa chosowa chilungamo; ndipo adzazunzika ndi moto komanso mwala wa safa pamaso pa angelo woyerwa, ndi pamaso pa NKHOSA: Ndipo utsi wa kuzunzika kwawo udzakwera kumwamba kwamuyaya: ndipo alibe tsiku lopuma kapena usiku wopuma, kwa iwo akutamandira chirombo [chirombo ndi U.N. ya Vatican, dziko la boma-limodzi, lotchedwa New World Order, lopangidwa ndi Cecil Rhodes] ndi chithunzi chake, ndiponiso aliyense wakulandira chizindikiro cha (Yapitilira pa tsamba 2)

<sup>1</sup> 1 Mafumu 22:19, Mas. 2:4, 9:4, 11:4, 47:8, 103:19, Yes. 6:1, 66:1, Dan. 7:9-10, Mat. 5:34-35, 23:21-22, Mac. 7:48-49, Chiv. 4:2-6, 9-10, 5:1, 6-7, 13, 6:16, 7:9-11, 15, 17, 12:5, 16:17, 19:4-5, 20:11, 21:5, 22:1, 3 2 Yoh. 3:5-6, 4:7-14, 7:37-39, Aef. 5:25-27, Aheb. 10:21-23, 1 Yoh. 5:5-8, Chiv. 21:6 3 Ezek. 36:27, Yoh 4:13-14, 14:15-26, 15:1-11, 26, 16:7-14, 17:20-23, 26, 1 Ako. 3:9, 16-17, 6:19-20, 2 Ako. 6:16-18, Agal. 2:20, Aef. 2:18-22, Afil. 2:12-13, Ako. 1:27-29, 2 Tim. 1:14, Chiv. 21:6, 22:17 4 Yob 19:25-27, Mas. 17:15, 49:15, Dan. 12:1-3, Hos. 13:14, Mat. 3:11-12, 8:11-12, 13:24-43, 25:30-46, Yoh. 5:21-29, 6:39-54, 11:23-27, Mac. 24:14-15, Arom. 8:10-23, 1 Akor. 6:14, 15:35-54, 2 Akor. 4:14, Chiv. 20:11-15, 21:8

# KHRISIMASI NDI CHIPULUMUTSO

(Yachokera pa tsamba 1)

dzina lake." Aliyense wodzitangwanitsa ndi boma la nkhanza zoyipitsitsali, limene MULUNGU amadana nalo, alapiletu nthawi yomwe ino za tchimo limeneli, kenako akhale wobadwanso mwatsopano mwa MZIMU, mtsinje wa MOYO, ndikuyamba kutumikira MULUNGU.

Kenango, MULUNGU anakanzekera kutumiza MWANA WAKE yekhayo wokondedwa kuchoka ku mpando wa MULUNGU kupita muchibelekero cha Maria, mwa MZIMU WOYERA, mtsinje wa MOYO, kudzakhala MULUNGU-MUNTHU oyamba (Adamu otsiriza). "Ndipo kwalembedwa choncho, munthu woyamba Adamu anakhala mzimu wamoyo; Adamu wotsirizayo analengedwa MZIMU wachangu [WAKULENGA-MOYO]" (1 Akorinto 15:45). Uku kunali kupereka mwayi wachiwiri kwa anthu kuti asiye moyo wauchimo, kuchoka munsinga za Satana, komanso kuchoka mu Gehena wa tuyaya, mu Nyanja ya Moto ndi mazunzo.<sup>5</sup>

KHRISTU, amene ali MAWU a MULUNGU, adzabadwa muthupi mosiyana ndi wina aliyense. IYE adzakhala munthu, koma IYE adzakhala osachimwa chifukwa IYE anadza mwa MZIMU WOYERA, mtsinje wa MOYO kuchoka ku mpando wa chifumu wa MULUNGU.<sup>6</sup> MPULUMUTSI wa MULUNGU anachoka kumwamba kudzakhala MWA-NA wa MULUNGU muchiberekelo cha namwali.<sup>7</sup> Mbiri ikuti Mariya anali ndi zaka pakati pa 9 ndi 10 pamene anatenga pakati popanda chodetsa pa YESU muchiberekelo chake.

Panali kukhuthuka kwa MZIMU WOYERA wa MULUNGU munthawi imeneyo womwe udakalipobe mpaka lero. Kukhuthuka kwa MZIMU WOYERA kunaloseled-

## Okondeka Tony Alamo Ministries,

Alemekezeke Ambuye. Ndikhulupilira muli bwino mwa Khristu. Ndine okondwa kugawana nanu zomwe ndaphunzira mwa Mulungu ndi ulendo wanga wa Uthenga Wabwino. Tsiku ndi tsiku tikukula mwa Khristu ndikupanga anthu kukula mwa Mulungu wathu. Posachedwapa gulu lathu la Alamo linapita kualalikira Uthenga Wabwino ndipo linakwaniritsa kufalitsa Uthenga Wabwino. Ena mwa ma pologalamu athu amatchingidwa ndi Satana ndipo analenga mavuto ena azachuma, koma tinagonjetsa ndi pemphero. Apa zozizwitsa zambiri zinachitika ndi Mzimu Woyerwa wa Mulungu. Munthu wina m'tchalitchimo m'moyo wake waukalamba anamanga makachisi ndi mafano, koma pano anatembenukila kwa Yesu. Amabwera ku tchalitchi nt hawi ndi nthawi ndipo amakonda kumpemphera. Tikuwalitsa zolemba ndi ma umboni a m'busa wathu Tony Alamo kwa anthu ambiri. Ndizosangalatsa kuti anthu amudziwe Yesu.

wa ndi mneneri Yoweli mu Yoweli 2:28-31: "Ndipo kumapeto ake kudzachitika, ndipo ndidzatsanulira MZIMU WANGA pa anthu onse, ndi ana anu amuna ndi akazi adzalosera, akuluakulu anu adzalota maloto, achinyamata adzaona maso mphenya: ndipo pa antchito anu ndidzakhuthula MZIMU WANGA m'masiku amenewo. Ndidaonetsa zoda bwitsa kumwamba ndi dziko la pansi, mwazi ndi moto, ndimizati ya utsi. Dzuwa lidzasinthidwa kukhala m'dima, ndipo mwezi kukhala mwazi, lisanafike tsiku lalikulu ndilowoppsa la AMBUYE." Aliyense ankayembekezera MESIYA wa MULUNGU kuonekela pa nthawi imeneyo.

YESU anali munthu oyamba kubadwa mwa mtsinje wa MOYO (MZIMU WOYERA). Kuti aliyense apulumuke kapena apitilize kukhala opulumutsidwa mwa MZIMU WOYERA, aliyense ayenera kumwamu mtsinje kudya kuchoka mu mtengo

Zikomo kwambiri pondipatsa mwayi wofalitsa Uthenga Wabwino ndi inu. Anthu ambiri amafunsa za mabuku ndi zolemba zina zambiri kuti afalitse. Ndadabwitsika ndi zozizwitsa za Mulungu.

Tikupempherera kutulutsidwa kwa m'busa Alamo kwa msanga. M'mapemphero athu a tsiku ndi tsiku, timapemphera kuti atulutsidwe m'dzina la Mulungu odziwa zonse. Sataya anthu ake. Tili pano kufalitsa mau ake kuti adziwike. Chokhacho chomwe tilinacho m'dziko lapansili ndi mau a Mulungu. Salephera, tsono tisataye chikhulupiliro, ndipo tisadumphe mau a Mulungu.

Chonde tumizani malembo ndi mabuku ena. Zidzalimbikitsa gulu lathu kupanga zinthu zabwino zambiri kwa Mulungu. Alemekezeke Ambuye. Chonde tumizani malembo ndi ma Baibulo ambiri kuti tilimbikitse gulu langa. Zikomo.

Darakonda Sagar  
Andhra Pradesh, India

wa MOYO tsiku lonse.<sup>8</sup> Muyeneranso kudya masamba amu mtengo wa MOYO tsiku ndi tsiku ndicholingga chopulumutsa mitundu, apo ayi mudzafa ndithu.

Genesesi 2:17, MULUNGU anati tsiku lomwe mudzadye kuchoka mumtengo wozindikila zabwino ndi zoipa (dziko), "mudzafa ndithu." Pamene simukudya kuchoka mu mtengo wa MOYO, ndikumwa kuchoka mu mtsinje wa MOYO tsiku lonse, ndiye kuti mukudya kuchoka mumtengo wa kuzindikila zabwino ndi zoipa, zomwe zikutanthaiza kuti mudzafa ndithu. Izi zikuchokera kwa MULUNGU, ndipo MULUNGU sanganame.<sup>9</sup> Aheberi 6:18 akutsimikiza mfundo imeneyi, kunena "Kuti mwa-zinthu ziwiri zosasinthika, mmene MULUNGU sanganame, tikakhale nacho chotichenjeza cholimba, ife amene tidathawa kuchigwira chiyembekezo choyikika pamaso pathu." Zinthu ziwiri zosasinthikazi ndizoti

<sup>5</sup> Luka 24:46-47, Yoh. 12:23-24, Mac. 26:15-18, Arom. 5:6-21, 8:32-34, 1 Akor. 15:45-57, Agal. 4:4-5, Aef. chap. 2, Ako. 1:12-14, 1 Ates. 1:9-10, Aheb. 9:13-15, 1 Pet. 1:3-5, Chiv. 1:18 <sup>6</sup> Yes. 7:14-15, Arom. 8:3, Afil. 2:6-8, Aheb. 2:16-18, 4:14-15, 5:8-9, 7:26-28, 9:14, 1 Pet. 1:18-19, 2:22, 1 Yoh. 3:5-6, Chiv. 5:1-10 <sup>7</sup> Yes. 7:14, Mat. 1:18-25, Luka 1:26-37 <sup>8</sup> Det. 8:3, Yos. 1:8, Yes. 55:1-3, Mat. 4:4, 5:6, 26:26-28, Yoh 4:10, 14, 6:31-35, 48-58, 63, 7:37-39, 2 Tim. 2:15, 3:14-17, Chiv. 21:6, 22:1-2, 17 <sup>9</sup> Num. 23:19, Det. 7:9-10, 32:4, Yos. 23:14-16, 1 Sam. 15:29, Mas. 36:5, 89:34, 100:5, 105:7-10, Yoh. 17:17, Arom. 3:4, 1 Ates. 5:24, 2 Tim. 2:13, Tit 1:1-2, Aheb. 6:10-19

## India



*M'busa Karumanchi  
Prakasarao ndi timu yake  
kugawa zolemba za Uthenga  
Wabwino za M'busa Alamo  
m'dera la Ramanakkapeta,  
Andhra Pradesh, South India*

tidye kuchoka mumtengo wa MOYO tsiku lonse tsiku ndi tsiku ndikumwa kuchoka mu mtsinje wa MOYO, umene uli MZIMU WOYERA, tsiku lonse tsiku ndi tsiku.

Yesaya 7:14 amati "Pamenepo AMBUYE MWINI adzakupatsani chidzindikiro; Taonani namwali adzakhala ndi pakati, ndipo adzabala MWANA wa MWAMUNA, ndipo adzatchedwa dzina lake Imanuweli." Ndiponso, Yesaya 9:6 akuti, "Pakuti kwa ife MWANA watibadwira, kwa ife MWANA wa mamuna wapatsidwa: ndipo ulamuliro udzakhala pa phewa LAKE, ndipo adzamutcha dzina LAKE WODABWITSA, WAUPHUNGU, MULUNGU wa MPHAMVU, ATATE WA MUYAYA, KALONGA WA MTENDERE."

"Ndipo Mumwezi wachisanu ndi chimodzi mngelo Gabrieli anatumidwa kupita ku mzinda wa Galileya ndi MULUNGU, wotchedwa Nazareti, Kwa namwali anakwatiwa [kutomeredwa] kwa [wachikulire, munthu wokhwima maganizo wotchedwa] Yosefe, wafuko la Davide; ndipo dzina la namwaliyo ndilo Mariya. Ndipo mngelo anabwera kwa iye, nati, Tikuoneni, wochitidwa chisomo, AMBUYE ali ndi iwe: uli odala mwa

akazi onse. Ndipo pamene anamuona iye, ananthunthumira ndi mawawa, nasinkhasinkha kulankhula uku nkotani. Ndipo mngelo anati kwa iye, Usaope, Mariya: pakuti wapeza chisomo ndi MULUNGU. Ndipo, tona, udzakhala ndi pakati, nudzabala MWANA WAMWAMUNA, nudzamutcha dzina LAKE YESU. IYE adzakhala wamkulu, nadzatchedwa MWANA WAMKURUKURU: ndipo AMBUYE MULUNGU adzampatsa IYE mpando wachifumu wa Davide atate WAKE: Ndipo IYE adzalamulira pabanja la Yakobo kunthawi zonse; ndipo ufumu WAKE sudzatha.

"Ndipo Mariya anati kwa mngelo, Ichi chidzachitika bwanji, popeza ine sindidziwa mwamuna? Ndipo mngelo anayankha nati kwa iye, MZIMU WOYERA udzafika pa iwe, ndi mphamvu ya WAMKURUKURU idzakuphimba iwe: kotero kutinso CHOYERACHO chikadzabadwa chidzatchedwa MWANA wa MULUNGU" (Luka 1:26-35).

Panaliso maulosi ena okwana 333 okhudzana ndi kubwera koyamba kwa KHRISTU womwe anakwaniritsidwa pa tsiku la Khrisimasi ndi masiku wonse a MOYO WAKE.<sup>10</sup> Anthu ambiri adzikolo lapansi ankadzi-

wa zochepta zamaulosi amenewa. Ngakhale Mfumu yoipa Herodi inkawadziwa ena mwa iwo, monga kubadwa kwa KHRISTU ku Bethlehemu ku Yudeya. Pamene Mfumu yoipa Herodi inasonkhanitsa ansembe ndi alembi pamodzi, inawafunsa zakomwe KHRISTU adzabadwire. Ndipo anati kwa iye, M'Bethlehemu wa Yudeya: chifukwa kunalembedwa ndi mneneri kuti, Ndipo iwe Bethlehemu, dziko la Yudeya, sukhala konse wamng'onong'ono mwa akulu a Yudea: pakuti Otsogolera (Gavana) adzachokera mwa iwe, amene adzawete anthu ANGA a Izrayeli. Kenako Herodi, pamene anayitana anzeru akummawa, anawafunsitsitsa za nthawi yomwe nyenyezi inawawonekera. Ndipo anawatumiza ku Bethlehemu, nati, Pitani ndipo mukafufuze za KAMWANA; ndipo mukakamupeza IYE, mudzandiuze, kuti nanenso ndipite ndikamulambire IYE. Atamva kuchoka kwa mfumu, ananyamuka; ndipo, taonani, nyenyezi, imene anayiona kum'mawa, inawala patsegolo pawo, mpaka kukafika ndi kui-ma pamene panali KAMWANA. Pamene anaona nyenyezi, anasangalala kwambiri. Ndipo pamene analowa

(Yapitilira pa tsamba 4)

<sup>10</sup> Mesiya Malingana ndi Ulosi waru Baibulo ndi M'busa Tony Alamo

# KHRISIMASI NDI CHIPULUMUTSO

(Yachokera pa tsamba 3)

mnyumba, anaona KAMWANA kali ndi Mariya mai AKE, ndipo anagwada pansi ndikumulambira IYE: ndipo pamene anatsegula chuma chawo, anamupatsa IYE mphatso; golide, ndi libano, ndi mure.

“Ndipo iwo pakuchenjezedwa m’kulota kuti asabwerere kwa Herodi, anachoka kupita kudziko lawo pa njira ina. Ndipo pamene iwo anachoka, onani, mngelo wa AMBUYE anaoneka kwa Yosefe m’kulota, nati, Tauka, nutenge KAMWANA ndi amake, nuthawire ku Aigupto, nukhale kumeneko kufikira ndidzakuza iwe: pakuti Herodi adzafuna KAMWANA kukaononga IKO. Ndipo iye ananyamuka, natenga KAMWANA ndi amake usiku, nachoka kupita ku Aigupto: Nakhalabe kumeneko kufikira atamwalira Herodi: kuti chikachitidwe chonenedwa ndi AMBUYE mwa mneneri, kuti, Ndinayitana MWANA WANGA atuluke m’Aigupto.

“Pamenepo Herodi, poona kuti anamupusitsa anzeruwo, anapsa mtima, natumiza ena, kukaononga tiana tonse ta mu Bethelehemu, ndi ta m’miraga yake yonse, takufikila zaka ziwiri nditating’ongo tonse, monga mwanthawi imene iye anafunsa kwa anzeruwo. Pomwepo chinachitidwa chonenedwa ndi Yeremiya mneneri, kuti, Mau anamveka m’Rama, maliro, ndi kulira kwambiri, Rakelo wolira ana ake, ndipo wosafuna kuthothozeka, chifukwa iwo palibe” (Mateyu 2:4-18).

Antru ambiri samulandira YESU kapena kupitiliza mwa IYE chifukwa choopa kuzunzidwa ndi kusowetsedwa mtendere.<sup>11</sup> Mateyu 13:20-21 akuti, “koma iye amene AFESEDA pa miyala [ouma mtima], uyu ndiye wakumva MAU, ndikuwalandira pomwepo mwamsangala; ndipo alibe mizu mwa iye, koma akhala nthawi yochepa: ndipo pakudza

msawutso kapena zunzo chifukwa cha MAU, iye akhumudwa pomwepo”—ndipo nditha kuwonjezera, kuopa. Anthu akhonza kunena, “Oh! Oh! Sindimafuna zimenezi! Ndima-funa kupindula ndi ulemelero ndi mphoto zachipulumutso, koma osati izi (mazunzo ndi kusowa mtendere).” Choncho amachoka kwa AMBUYE, ndikukhala mu Nyanja ya Moto, zimene zili zowawa kwambiri kuposa mazunzo ndi kusowetsedwa mtendere. Tonse tithokoze MULUNGU kuti YESU, Mariya ndi Yosefe sanagwe chifukwa chakuzunzika ndi kusowetsedwa mtendere kumene anakumana nako.

Patsiku la Khirisimasi, MPULUMUTSI anabadwa. Ngakhalenso kuposa MPULUMUTSI, MLENGI wa Kumwamba ndi dziko lapansi anabadwa kuthupi.<sup>12</sup> IYE analenganso dzuwa, mwezi, gulu la nyenyezi, maiko, ndi nyenyezi, mpweya, mphamu yokokera zinthu pansi, zazin’gonozin’gono zonse (atom), ndi zochepesetsa zonse (molecule). Yohane 1:3-5 akuti, “Zonse zinalengedwa ndi IYE; ndipo kopanda IYE zinthu zonse zomwe zinalengedwa bwenzi kulibe. Mwa IYE munali MOYO, ndipo MOYO umenewu unali KUUNIKA kwa anthu. Ndipo KUUNIKA kumeneneko kunawala mu mdima [dziko la mdimali]; ndipo mdimawu sunakuzindikile [anthu a dziko lapansi okonda zamu mdima, sangathe kumvetsa zinthu zamphamu ya uzimu].”

Antru akamaona masomphenya a KHRISTU atakhala pa mpando WAKE wachifumu Kumwamba (ndipo tiyenera kukhala ndi masomphenya, kupanda apo tonse titha<sup>13</sup>), timawuona mtsinje umenewu wa madzi a MOYO “wotuluka kumpando wachifumu wa MULUNGU ndi wa NKHOSA [mpando WAKE wachifumu]. Pakatikati panjira yake, komanso mbali zonse za mtsinje, kunali mtengo wa MOYO [chimene chilinso chizindikiro cha YESU, MAU a MULUNGU], womwe uma-

bala mitundu khumi ndi iwiri ya zipatso, ndikukoloredwa zipatso zake mwezi ndi mwezi; ndipo masamba ake ndiwo machiritso adziko lapansi” (Chivumbulutso 22:1-2).

Maganizo a munthu sangathe kumvetsetsa ndipang’ono pomwe mmene mphamu ya MULUNGU ikuchitira zinthu, makamaka zonse zomwe IYE akupanga panthawi imodzi. Ndiyamba ndi mmene IYE amathanirana ndi mayesero ndi kusowa mtendere kwa munthu aliylene, kudwala kwavo, matenda, ndizofooka, chimwemwe ndi chisoni, kubadwa kwavo ndi kufa kwavo, machiritso awo, mapemphero awo, kutumikira kwavo ndi kalandira MAU AKE, nkhondo zawo ndi mphekesera za nkhondo zawo. Palinso machitidwe AKE amene amathanirana ndi anthu omwe akulingalira zakupha anzawo, kutaya mimba, kudzipha, ndi machimo ena onse monga kugonana kwa amuna kapena akazi okhaokha, chiwerere, chisembwere, ukwati wa akazi okhaokha, komanso anthu kugonana ndi zinyama. MULUNGU akudzia ndithu za udzu uliwonse, komanso china chili chonse chokhudza mbalame, nsomba iliyonse, nyama iliyonse, ndi munthu aliylene. Amadziwa zamaganizo a munthu aliylene ndi zofuna za munthu aliylene. IYE amadziwa nthawi yomwe wamuika IYE pambali ngati opanda phindu.<sup>14</sup>

Pali fanizo lokhudzana ndi izi mu Baibulo. Ndi fanizo la mbeu ya mpiru, yomwe YESU anawaonetsera anthu, nati, “Ufumu wa Kumwamba [MAU a MULUNGU] uli ngati mbewu ya mpiru [anthu a dziko lapansi amatenga MAU a MULUNGU, Ufumu wa Kumwamba, ngati opanda ntchito,

<sup>14</sup> 1 Sam. 16:7, 1 Maf. 8:39, 2 Maf. 19:27, 1 Mbi. 28:9, Yob 31:4, 34:21-22, 25, Mas. 44:21, Mas. 50:21-22, 139:1-6, 12-16, Miy. 1:25-33, 15:3, 11, Yes. 42:9, Jer. 16:17, Ezek. 11:5, Mat. 6:8, Luka 16:15, Mac. 15:18



wochepetsesa pa zonse, wochepetsesa kuposa mbeu zonse (MAU)], zomwe munthu anatenga, ndikudzala m'munda mwake [mumtima mwake]: Yomwe ndithu [mbeu ya mpiru] ndi yaying'ono pa mbeu zonse: koma ikakula, imakhala yayikulu kuposa masamba wonse, ndikukhala mtenago, koteru kuti mbalame za mlengamenga zimadza, nizibindikira mu nthambi zake" (Mateyu 13:31-32).

Pamene MAU a MULUNGU mwa chikhulupiliro alowa mumtima mwa munthu, amasandu-liko mtengo waukulu, chifukwa munthu yemwe ali ndi chikhulupiliro amayamba kufalitsira MAU a MULUNGU kutali, ndipo tchalitchi chimabadwa kuchokera mwa iye. Choncho, ngati tchalitchi chabadwa, chimakhala nyumba ya anthu ambirimbiri. Anthu ena odzadzidwa ndi mphamu yaziwanda amalowa pang'opang'ono mutchalitchi, kuyesera kuononga podzala chiphunzitso chabodza komanso kumadzdzula mwabodza atsogoleri pakutumikira kwawo kwa Satana.<sup>15</sup>

Ziwanda mu fanizo limeneli zi-kuyelekezedwa ngati mbalame za mlengalenga zimene zimadza nizibindikira munthambi zake. Zili mu matchalitchi onse achilungamo. Ntchito za Satana ndikulepheretsa ntchito za MULUNGU mu njira ina iliyonse imene amadziwa, ndipo akudziwa njira zambiri zosiyanasiyana.<sup>16</sup> Ali ndi zaka 7,000 za ukadaulo. Ichi ndichifukwa chake tiyenera kukhala ndi maganizo a KHRISTU (1 Akorinto 2:16) ndi zida zonse za MULUNGU (Aefeso 6:11) kuti tikwanitse kulimbana ndi machitidwe a ukamberembere wa m'dierekezi.<sup>17</sup> 1 Petro 5:8 akuti, "Khalani atcheru, dikirani; chifukwa m'dani wanu mdierekezi, monga mkango wobuma, ayendayenda, ndi kufunafuna wina amlikhwire." Koteru, "Dziperekeni kwa MULUNGU. Mukaneni mdierekezi, ndipo adzakuthawani inu" (Yakobo 4:7).

<sup>15</sup> Dan. 11:30-32, Mat. 7:13-23, 10:16-18, 21-28, 13:24-31, 36-43, 47-50, 24:9-12, Mac. 20:28-31, Agal. 2:3-5, 2 Pet. chap. 2, 1 Yoh. 2:18-19, 4:1-6, 2 Yoh. 7-11, Yuda 3-19 **16** Yes. 14:4-20, Mat. 24:24, Yoh. 8:44, 10:10, 2 Ako. 4:3-4, 11:13-15, 2 Ates. 2:3-12, 1 Pet. 5:8, 1 Yoh. 4:1, Chiv. 2:9, 12:9, 13:1-8, 11-14, 16:13-14, 20:8-15 **17** 1 Ako. 2:11-16, 15:57-58, 16:13, 2 Ako. 6:1, 4-7, 10:3-6, Aef. 4:27, 6:10-18, Afil. 2:5, 1 Ates. 5:3-9, 21, 1 Tim. 6:12, 2 Tim. 2:3-4, Aheb. 4:12, 12:1-4, Jas. 4:7, 1 Pet. 5:8-10, 1 Yoh. 5:4 **18** Det. 31:21, 1 Sam. 16:7, 2 Maf. 19:27, 2 Mbi. 16:9, Mas. 7:9, 66:7, 139:1-6, 12-16, Yes. 29:15-16, 46:9-10, 48:5, Jer. 1:5, Amos 9:1-4, Luka 12:2-7, Arom. 8:27-29, 1 Yoh. 3:20

## Missouri

Okondeka M'busa Alamo,

Chisomo ndi kudzodza kwa Mulungu komwe kumaposa zonse zakumvetsa ndi kudziwa kudzera mwa mwana wake Yesu Khristu zikhale nanu ndi utumiki wanu. Ndinayimba foni mu November ku laini ya kochitila umboni kupempha pemphero lokhudza mkazi wanga; ali ndi khansa. Ndathana ndi mavuto ambiri okhudza mtima. Mapemphero anu ndiothandiza kwambiri kwa ine ndi banja langa. Ndimapemphelera usiku ndi usana okondedwa anga pamodzi ndi m'busa Alamo. Mwakhala mukundithandiza pondilola kufika pamwambamwamba pa kuzindikira za uzimu. Ndi kudziwa kuti mzimu wanga unatembenukila kwa Ambuye chifukwa cha zinthu zomwe munanditumizila. Ndawadziwitsa anthu ambiri za inu. Zikomo kwambiri chifukwa cha thandizo lanu. Ndikupemphera kuti Ambuye ndi Mpulumutsi wathu anditulutse kundende kuno. Ndikudikilira tsiku lokhululukira akaidi mu February. Ndikupemphera kuti nanunso mutulutsidwe posachedwa.

Robert Green

Farmington, MO

Zimaoneka ngati ntchito kwa anthu amdziko lapansi kudziletsa kuchita zichitochito za dziko lapansili. Amaona chovuta kuti aziganizira za ufu-mu wa MULUNGU, KHRISTU ndi ATATE AKE amene amakhalapo, ndi MIZIMU ya MULUNGU isanu ndi iwiri, imene ili maso a MULUNGU amene anatchulidwa mubukhu la Zakariya, chapatala 4, vesi 10: "Isanu ndi iwiri imeneyo [MIZIMU ya MULUNGU]; ndi maso a AMBUYE, amene amaona uku ndi uko padziko lonse lapansi." Komanso, Yesaya 11:2 akutchula maina a MIZIMU ya MULUNGU isanu ndi iwiri, amene ali 1) MZIMU wa MULUNGU, 2) MZIMU wa nzeru, 3) MZIMU wa kuzindikira, 4) MZIMU wa uphungu, 5) MZIMU wa mphamu, 6) MZIMU wa kudziwa, ndi 7) MZIMU wa kuopa AMBUYE

Chivumbulutso 1:4 akuti, "Yohane kwa mipingo isanu ndi iwiri m'Asia [Turkey]: Chisomo kwa inu, ndi mtendere, zochokera kwa IYE amene ali, ndi amene adali, ndi amene ali nkudza; ndi kwa MIZIMU isanu ndi iwiri yokhala ku mpando wa chifumu WAKE." Ndipo Chivumbulutso 3:1 akuti, "Zinthu izi anena IYE [YESU] wakukhala nayo MIZIMU ya MULUNGU isanu ndi iwiri, ndi nyenyezi zisanu ndi ziwiri."

Ndi zinthu zonse zonyasa zochitika m'dziko, mutha kukhala osadziwa kuti MULUNGU amadziwa chili chonse chomwe chikuchitika padzikolo lonse lapansi, kape-na kuti MZIMU WAKE umadziwa chenicheni chomwe mukuganiza ndi komwe muli. IYE amadziwa chili chonse cha inu.<sup>18</sup> Vuto ndilakuti simukudziwa kuti MULUNGU akuthira mtsinje WAKE wa MOYO, MZIMU WAKE wa MOYO, pansi kwa inu kuti mulandire ngati MOYO wanu wosatha. Muli ndi moyo wonggwilizira, womwe utathe mwamsanga, mwina mwamsanga kuposa momwe mukuganiza. Komabe, MULUNGU akufuna inu kuti mulandire MOYO WAKE wamuya-aya mu mzimu wanu wa umunthu wamuyaya kuti mukhale kwamuyaya ndi IYE Kumwamba.

Muli ndi thupi, moyo, ndi mzimu. Baibulo likunena kuti thupi silipindula kanthu (Yohane 6:63), ndipo moyo wochimwa ukuyenera kusalidwa, koma mzimu wanu—mukufuna MOYO wosatha—ulandire MZIMU wa MOYO wa KHRISTU mwa iwo. Mtsinje wa MOYO wosatha ukudikira inu kuti mulandire MOYO, umene uli KHRISTU

(Yapitilira pa tsamba 8)

# UMBONI WA TERRI WHITE

## *Chozizwitsa cha Mamasulidwe*


Sindinachokere ku nyumba yophothyoka yozunguliridwa ndi zisawawa, chisokonezo, mowa, kapena mankhwala osokoneza bongo, koma ndinaleredwa ndi makolo achikondi, wondisamalira amene anaperekayo moyo wawo kusamalira m'chimwene wanga ndi ine. Tinali wokondwa chibwana chathu, kuwedza nsomba, kukwera abulu, kugona kunja mmatenti komanso kuchita masewera a m'madzi kumapeto kwa sabata.

Inali isanafike nthawi ya Khrisimasi yanga yachisanu ndi chitatu pamene ndinalandira Baibulo langa loyamba kuchokera kwa agogo akazi. Pozindikira kuti ili linali bukhu lamtengo wapatali, ndinadzipatula ndekha ndikuliwerenga mwachidwi. Ili silinali bukhu longokhala ndi nkhani za Yesu. Mphamvu imene Yesu anali nayo pa anthu owawidwa mtima, zozizwa, chiyembekezo, komanso mtendere womwe Iye anawasiyira anthu nthawi imeneyo, zinandipangitsa kuganiza, "Oh, ndikanakhalapo nthawi imeneyo, ndikanamutsatira Yesu." Ndipo ndinakhumudwa kwambiri chifukwa Yesu wam'Baibulo ameneyu sanali mboni m'dziko lino lomwe ndimakhala.

Bambo anga anakumana ndi zovuta kwambiri ndi anthu otchedwa atsogoleri a chipembedzo, ndipo sanapitenso ku kachisi, kufikira nthawi imene ndinalandira chipulumutso zaka zambiri zotsatira pamene anabwera ku mpingo wachiKhristu wa Tony ndi Susan Alamo. Zotsatira zake, m'chimwene wanga ndi ine anakatisiya ku Sande sukulu. Zochepa zomwe tinaphunzira ndi tchalitchi cha Baptist ndizoti tikuyenera kuti tipulumutsidwe, ndimaganiza, kuti tisapite ku Gehena. Anthu oyipa monga okuba, okupha, ankhanza, ndi ena otero, adzapita kumeneko, osati anthu ngati ife. Ndimadzitangwanitsa ndi kukwera abulu komanso kuonetsa mphoto yanga ya kavaloo wokhala ndi maonekedwe ofira

moderako komanso khosi ndi mchira woyer (palomino) mzionetsero. Am-aonetsetsa kuti wabweretsa mariboni a blue; amapatsa chidwi aliyense pachionetseropo! Tsiku lina tikupita kuchionetsero chachikulu chaperete, tinapanaga ngozi ndipo bulu wanga, Amigo, anaphedwa. Ndinakhumudwa; maloto anga anathera pompo. Zinditengera nthawi mtsogolo muno ndisanayambenso kuchita za abulu.

Anzanga kusukulu amandinyengeleru munjira zonse kuti ndizigwiritsa ntchito mankhwala wozunguza bongo omwe anali atatenga malo kwambiri. Nditatsiriza maphunziro a sekondale, makolo anga anatisamutsira ku malo abwino. Tinasamukira ku Mapiri a Miyala (Rocky Mountains)aku Colorado kufupi ndi Mtsinje wa Little Cimarron. Tinazunguliridwa ndi nyanja, mitsinje, mapiri, komanso mapiri okhala ndi pamwamba pafulati m'mbali zathu zonse. Malo ogonapo apafupi osakirako nyama anali patsidya pa nyanja, ndipo amatchuka ndi nkhani zosaka nyama ndi kuwedza nsomba. Anandipatsa ntchito pamalo ogonapowo ngati wothandiza anthu pamalopo pazimene abwelera. Ndimatha maola ambiri kusamalira abulu apamalopo amene amagwiritsa ntchito pamaulendo okasaka. Tsiku lina lake ndinakwera ndekha, ndipo ndinafika malo otalikitsitsa a West Mesa. Pamene ndimafufuza kukongola kwa malowa, ndinadabwitsika ndi mitengo ya aspen ya masamba a golide, kuthetheka, fungo lamphamvu la paini, chewo chokhulira cha orange, ndi mitsinje yothamanga, yaukhondo kungomvera fungo lake. Mafunsowa amandizunguza: Zonse zokongolazi zolengedwa ndi Mulungu, koma ndichifukwa chiyani sindili okongola chonchi mumtimu mwanaga? Chifukwa chiyani maganizo anga komanso zikhumbokhumbo zanga zili zoipa, zodzikonda, ndi zopanda pake? Ndi chifukwa chiyani ndimak-



Mcchemwali Terri White

hala ngati ndili ndi nyama ya m'tchire mkati mwanga? Ndimakhala wokhumudwa komanso ndi mafunso ambiri.

Mosadziletsa kapena kuganza, ndinapondaponda anthu onse amene amandikonda. Ndinachoka wosayang'ananso m'mbuyo. Chaka chinacho sindinapezeke nkomwe ndikusokonekera kwa dziko lomwe linandizungulira. Palibe chomwe ndimaona chopelekera kumoyo wanga kapena chokonzeru moyo wanga. Ndinayendayenda mzinda ku mzinda, boma ku boma, kuchoka kugulu lochita zamankhwala ozunguza bongo ili kupita kulina. Ndinamwa mowa ndi mankhwala ndi chamba zokwani-ka kupha munthu aliyense wabwin-obwino. Koma chenicheni chimene chinanditsegula maso chinabwera patachitika zambiri zimene zikanan-disiyitsa mchitidwe wanga woipa. Komabe ndinapulumuka nditamwa mankhwala ozunguza bongo oposa muyezo, kuphulika kwa moto, ngozi ya bwato, komanso kutengedwa mokakamizidwa pokwera matola. Ndinapulumukanso pamene ndinkafuna kuwombera munthu amene anam'menya m'chimwene wanga. Zochitika zomalizazi ndizimene zinandipangitsa kuzindikira kuti sindimachita zinthu zoyenera. Mulungu anakwiya nane ndithu ndipo ndinadziwiratu kuti ndaponyedwa kale ku Gehena. Zi-

kanatheka bwanji kuti ndibwenzeretse pa ine mwini ndi miyoyo imene ndinayiwononga?

Ndinabwera ku Hollywood, CA, ndicholinga chimodzi kuti ndipange ndalamala ndikupita kuhiri kuti ndikabisale kuzovuta zamoyo zomwe zinadizungulira. Ndinadana nawo mzinda, makamaka Hollywood. Ndinadziwa nditangofika kuti ndasokoneza. Ndalamala zomwe ndinapeza zinabedwa, ndipo ndinadelera kuwayimbira makolo anga kuti andithandize. Ndipo ndinali ndi mantha kuti ndikwere matola; ndinapanikizika ngati khoswe. Kenako sabata yotsatirayo pa Sunset Strip, ndinakumana ndi magulu a anthu achichepere omwe amaoneka ngati aliyense, koma zochita zavo zinali zosiyana ndi ena. Ana ogona m'misewu amawanyogodora powatchula kuti "Gulu la Mulungu." Pamene anthu omwewa anayankhula nane, anayankhula mwa ulamuliro komanso mokhudzidwa. Sizikanatheka kusemphana ndi kufunikira kwa uthenga wawo. "Yesu Khristu akubweranso padziko lapansi. Lapani kapena wonongekani. Pangani bata ndi Mulungu pamene nthawi ilipo. Yesu akubweranso ku dziko lapansi ndi ndodo yobwenzera kwa iwo wonse osamudziwa Iye. Gehena ndi wamuya. Tikukhala m'masiku otsiriza. Chitani ubwino ndi Mulungu nthawi isanathe. Bwerani kumapemphero akutchalitchi amene timakhala nawo usiku uliwonse ndikudziwa zambiri."

Liwu lakuti "Gehena" limandilasa mtima chifukwa ndimadziwa zinali zowona. Linalembeka mokwenza ndi momveka. Nthawi yomweyo china chake mkatı mwanga chinayankhula kuti, "Nthawi zonse umanena kuti ndiwe ofunafuna choonadi. *Pita ukafufuze za ichi.*" Patapita sabata imodzi ndinapeza chokwera changa ndikubwera kumapemphero aku tchalitchi pa Crescent Heights Blvd. ku Hollywood. Panali pa 9 November, 1970. Chimatchedwa Tony and Susan Alamo Christian Foundation. Sindikanakana Mzimu wachikoka ndi wamphamu, umene umandikoka, ngakhale chikayiko ndikutaya chikhulupiliro kunakuta maganizo ndi mtima wanga. Izi zinali zotsatira zachilengedwe zot-

sutsana ndi ukamberembere, maboda-za, ndi nkhanza za umunthu zimene zinandipweteka. Mosowa mtengo wogwira ndinabereda unyamata wanga, zimawoneka ndinali mwini wa nkhani yokhumudwitsa. Ndinadzidzudzula ndekha chifukwa cha maganizo oipa amene ndinasankha kuchita.

Pamene ndimalowa, m'chinyumba chachikulu chamasanja awiri chodzadza ndi anthu owoneka ngati mahippie, munali chimwemwe ndi chidwi zimene zinali zowonekeratu kwa ine. M'busa Tony Alamo amasowa mtendere kukhala pakati pa mahippie, chifukwa anavala suti yaubwana. Ndianaganiza zomuonetsetsa ndi china chili chonse chimene amafuna kuyankhula. Sindinakumane ndi mkazi wake Susan usiku umenewo. Mapemphero anayamba ndikuyimba nyimbo zauzimu zakalekale. M'zibambo anaimba "Ndi Mwana Wanji Uyu?" pa chitoliro, ndipo zimaoneka ngati mayimbidwe okomawa akuchokera kumwamba. Panalibe okestra yayikulu, koma china chake chimacheptsa mphamu yachitetezo yomwe ndinali nayo yomwe ndinamanga kuzungulira mtima mwanga. Misonzi inatsika m'masaya mwanga, ndipo ndinali kumva kwanthawi yoyamba Mzimu Woyer—a kudzadza m'moyo wanga wonse. Ndinali wochimwa wotayika wotsala pang'ono kupezedwa. Anthu obadwanso mwatsopano kumene anapeleka maumboni afupi, koma omveka bwino. Pakuyenera kuti panali maumboni opitilira 100 usiku umenewo. Panali oyimilira ochokera ku France, England, Canada, Australia, Mexico, South America, pafupifupi dziko lonse lapansi. Panalinso akuluakulu a misinkhu yapakati amene anasiya matchalitchi awo ozizira, akufa kudzalowa nawo m'mayendedwe abwino a Mulunguwa. Aliyense umboni wake unali wa phindu pokhanzikitsa chiyembekezo ndi chikhulupiliro mwa ine, komanso posenda khungu ndi khungu lachikaiko ndikupwetekela kwa mtima ndi mzimu wanga. Ndinamva za anthu okonda mankhwala osokoneza bongo atamasulidwa pompopompo ndi mphamu yachipulumutso ya Mulungu, komanso za zidakwa ziku-

pezeka opanda vuto lakusokonekera kwa mutu (delirium tremens). Bambo m'modzi ankapita kokaba kubanki pamene anayimitsidwa ndikutengeredwa ku tchalitchi kumene anakabadwanso mwatsopano, ndipo anapangidwa kukhala cholengedwa chatsopano atalandira Yesu kukhala Mbuye wake.

M'busa Alamo anabweretsa uthenga okhudza maulosi a nthawi-yotsiriza ndikuwerenga chaputara 24 cha Matheyu. Unali uthenga wauzimu wosavuta, uthenga wauzimu wodziwikiratu, olalikidwa mumphamu za Mzimu Woyer wa Mulungu. Ndingakane bwanji mayitanidwe okagwada kuguwa ndikuitanira Yesu mumtima mwanga? M'busa Tony nayenso anagwada ndikutsoglera pemphero la ochimwa malingana ndi Baibulo la KJV. Nditalapa ndikupempha Yesu kutsuka machimo anga ndi mwazi Wake wamtengo wapatali, ndikumuyitanira Iye mumtima mwanga, Iye anandikhululukira! Ndinali watsopano! Kupeze ka kwa chilungamo chokhala ngati chikhulupiliro cha mwana wakhanda kunadzadza mtima wanga. Chimwemwe, mtendere, ndi chiyembekezo zinasefukira mwa ine, kuposa mmene ndimayembekezelera. Ndinapangidwa cholengedwa chatsopano. Ndinamvetsetsa ndikulawa mphamu yachipulumutso, kumasulidwa kozizwitsa kumene Yesu Khristu yekha angapereke. Bambo wozizwitsa ameneyu wa Baibulo langa loyamba ngati mwana ndiwamoyo ndipo akugwira ntchito, kuyankhula ndikuyenda ndi iwo wonse amene atsegula chitseko cha mtima wawo.

Papita zaka zoposa 42 m'mene ndakhala ndikuchitira umboni komanso kuona mphamu ya machiritso, chiukitso, ndi chipulumutso. Ndaona zozizwitsa zambiri zamtundu wotere. Izi ndi zotsatira za nzeru zodzipereka za M'busa Tony ndi malemu mkazi wake Susan Alamo kuti awine miyoyo yambiri, ndikuyikhanzikitsa mu Mawu Oyera a Mulungu. Anatiphunzitsa makhwekhwe a maudindo a Satana ndikuwayika poyer a anthu okana Khristu onse. Ndikuthokoza kosalekeza. Kwa Mulungu kukhale ulemelero, ndipo ndithokoze okondedwa M'busa Tony Alamo.

# KHRISIMASI NDI CHIPULUMUTSO

(Yachokera pa tsamba 5)

YESU AMBUYE wanu. Choncho nenani pemphero ili:

**AMBUYE wanga komanso MULUNGU** wanga, ndichitireni chifundo ndine munthu wochimwa.<sup>19</sup> Ndiukhulupirira kuti YESU KHRISTU ndi MWANA wa MULUNGU wamoyo.<sup>20</sup> Ndimakhulupiriranso kuti IYE anafera pamtanda ndipo anakhetsa mwazi WAKE wamtengo wapatali ndi cholinga choti machimo anga onse akhululukidwe.<sup>21</sup> Ndiukhulupiriranso kuti MULUNGU anaukitsa YESU kwa akufa pogwiritsa ntchito mphamu ya MZIMU WOYERA,<sup>22</sup> ndiponso kuti IYE anakhala kudzanja lamanja la MULUNGU ndipo panopa akumva pemphero langa lolapali.<sup>23</sup> Ndiukutsegula zitseko za mtima wanga, ndipo ndikukuyitanani kuti mulowe mumtima mwanga, inu AMBUYE YESU.<sup>24</sup> Tsukani machimo anga ambirimbiiri achoke onse mu mwazi wamtengo wapatali umene INU munakhetsa m'malo mwanga pamtanda wa ku Kavari.<sup>25</sup> Ndiukudziwa kuti mundimvera pemphero langali AMBUYE YESU; INU mukhululukira machimo anga ndi kupulumutsa moyo wanga. Ndiukudziwa izi chifukwa MAWU ANU, Baibulo, limanena zimenezi.<sup>26</sup> MAWU ANU amati INUYO simudzakana kumvetsera pemphero la munthu aliyense, ndipo ine ndili m'gulu la anthu amenewo.<sup>27</sup> Choncho, ndikudziwa kuti INUYO mu-

kundimvetsera pamene ndikupemphera ndipo ndikudziwano kuti INUYO mundiyankha komanso mundipulumutsa.<sup>28</sup> Ndipo ndikukuthokozani AMBUYE YESU, chifukwa chopulumutsa moyo wanga, ndipo ndisonyeza kuyamikira mwa kuchita zinthu zimene INUYO munalamula komanso kupewa kuchita uchimo.<sup>29</sup>

Pambuyo pa chipulumutso, YESU ananena kuti munthu ayenera kubatizidwa pomizidwa thupi lonse m'madzi, m'dzina la ATATE, ndi la MWANA, ndi la MZIMU WOYERA.<sup>30</sup> Muziphunzira mwakhama Baibulo la *Buku Lopatulika Ndilo Mau a Mulungu*, [King James Version] ndipo muzichita zimene Baibulolo limanena.<sup>31</sup>

AMBUYE akufuna kuti inuyo muziwiza ena za chipulumutso chanu. Mungathe kukhala wofalitsa uthenga wabwino wa Mbusa Tony Alamo. Tizikutumizirani mabuku mwaulere. Imbani foni kapena tumizani imelo kwa ife kuti mudziwe zambiri. Tiku-kupemphani kuti muwuzeko ena uthengawu.

Ngati mukufuna kuti dziko lipulumutsidwe monga m'mene YESU akulamulira, mukufunika kuperekwa chakhumi kwa MULUNGU. MULUNGU anati, "Kodi munthu angabere MULUNGU? Inde, mwandibera kale. Koma akuti, Ife tikumubera bwanji MULUNGU? Mu chakhumi ndi mu zopereka. Anthuwo ndi otembereredwa chifukwa akundibera, ngakhale mtundu wonsewu [dziko lonse lapansi]. Bweretsani nonse chakhumi ['chakhumi' ndi gawo limodzi la magawo khumi (10%) ya malipiro anu] m'nkhokwe zanga n'cholinga choti pakhale nyama [chakudy cha Uzimu]

mu nyumba YANGA [anthu opulumutsidwa] kuti mundiyese, akutero AMBUYE wa MAKAMU, kuti muone ngati sindidakutsegulirani mazenera a Kumwamba ndi kukukhuthulirani madalitso amene mudzasowa malo owalandirira." Ndipo ndidzadzudzula anthu okudyerani masuku pamutu ndipo sadzawononga zipatso za nthaka yanu; ngakhalenso mphesa wanu sudzalephera kubala zipatso pa nyengo yake m'minda yanu, watero AMBUYE wa MAKAMU. Ndipo mitundu yonse idzakutchanu odala: chifukwa dziko lanu lidzakhala labwino, watero AMBUYE wa MAKAMU" (Malaki 3:8-12).

Ngati mukufuna kutumikira AMBUYE, mukhonza kutero ku tchilitchi kwathu ngati musunga malamulo.

Ndipo, monga YESU alamulira, khalani okopa-miyoyo. Mukhonza kutero pakukhala ogawa zolemba za M'busa Tony Alamo. Timapurinta zolemba za M'busa Tony Alamo m'zinenero zambiri, ndipo ndimazitumiza pa dziko lonse lapansi. Timagwiritsa ntchito mamiliyonu amadollar pa mapepala ndi kutumizira, koteru tiku-funa mapemphero anu komanso thandizo la ndalama.

Mulungu akutilamula kukonza ndikudzudzula ana athu.<sup>32</sup> Banja limalorewa ndi Mulungu nthawi imene munthu watha msinkhu pamene ana akula kukhala azibambo ndi azimayi. Kuletsa ichi ndi chipunkunziso cha am'dierekezi (1 Timothy 4:1-3). M'busa Alamo ali mundende chifukwa chakulalikira ndi kuchita zimene Baibulo likunena.

<sup>19</sup> Sal. 5:1, Aro. 3:10-12, 23   <sup>20</sup> Mat. 26:63-64, 27:54, Luka 1:30-33, Yoh. 9:35-37, Aro. 1:3-4   <sup>21</sup> Mac. 4:12, 20:28, Aro. 3:25, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 5:9   <sup>22</sup> Sal. 16:9-10, Mat. 28:5-7, Marko 16:9, 12, 14, Yoh. 2:19, 21, 10:17-18, 11:25, Mac. 2:24, 3:15, Aro. 8:11, 1 Akor. 15:3-7   <sup>23</sup> Luka 22:69, Mac. 2:25-36, Aheb. 10:12-13   <sup>24</sup> 1 Akor. 3:16, Chiv. 3:20   <sup>25</sup> Aef. 2:13-22, Aheb. 9:22, 13:12, 20-21, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 1:5, 7:14   <sup>26</sup> Mat. 26:28, Mac. 2:21, 4:12, Aef. 1:7, Akol. 1:14   <sup>27</sup> Mat. 21:22, Yoh. 6:35, 37-40, Aro. 10:13   <sup>28</sup> Aheb. 11:6   <sup>29</sup> Yoh. 5:14, 8:11, Aro. 6:4, 1 Akor. 15:10, Chiv. 7:14, 22:14   <sup>30</sup> Mat. 28:18-20, Yoh. 3:5, Mac. 2:38, 19:3-5   <sup>31</sup> Deut. 4:29, 13:4, 26:16, Yos. 1:8, 22:5, 2 Tim. 2:15, 3:14-17, Yak. 1:22-25, Chiv. 3:18   <sup>32</sup> Miy. 13:24, 19:18, 22:6, 15, 23:13-14, 29:15, 17, Aheb. 12:5-11, Chiv. 3:19

*Ngati mukufuna kudziwa zambiri kapena ngati mukufuna mabuku kapenanso nkhanzi zina zimene zimakusangalatsani, tiimbiren foni kapena tilembereni.*

**Tony Alamo, World Pastor, Tony Alamo Christian Ministries Worldwide • P.O. Box 2948, Hollywood, CA 90078**

**Twenty-four hour prayer and information line: (661) 252-5686 • Fax (661) 252-4362**

**www.alamoministries.com • info@alamoministries.com**

*Tony Alamo Christian Ministries Worldwide imalandira anthu onse ndipo imaperekwa zinthu zofunika Kwa onse amene ali ku U.S. amene akufunitsitsadi kuti ayambe kutumikira AMBUYE ndi mtima wawo wonse moyo wawo wonse ndi mphamu zavo zonse*

**Maservice amachitikira ku New York City lachiwiri lililonse nthawi ya 8 koloko usiku ndi malo ena usiku okhaokha.**

**Chonde imbani (908) 937-5723 kuti mudziwe zambiri. ZAKUDYA ZIMAGAWIDWA PAMAPETO PA MAPEMPHERO ALIWONSE.**

**Funsani buku la M'busa Alamo, lakuti Mesiya, losonyeza KHRISTU kuyambira ku Chipangano Chakale mu maulosi oposa 333.**

**Khalani wogwira ntchito yokolola miyoyo ya anthu pakukhala ogawira mabuku a M'busa Alamo  
Mabuku ndi zinthu zonse zomvetsera n'zaulere, ndipo simulipira ndalama yotumizira**

**Ngati wina akukuuzani kuti mupereke ndalama pa zinthu zimenezi, chonde imbani pa (661) 252-5686.**

**M'BUKU ILI MULI CHIKONZERO CHENICHENI CHA CHIPULUMUTSO (Machitidwe 4:12).**

**MUSALITAYE, PATSANI ENA KUTI AWERENG.**

**Anthu amene muli m'mayiko ena, tikukulimbikitsani kuti mumasulire n'chinenero chanu mabukuwa. Ngati  
mukusindikizanso bukuli, musaiwale kuika mawu ali m'munsiwa omwe ndi okhudzana ndi zamalamulo:**